

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

KODI NDINU NDANI?

(Nkhani ili mmunsimuyi ikunena zinthu zimene zinachitika pa Machitidwe 19:10-20).

Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu, anatumikira mu mzinda wa Efeso kwa zaka ziwiri. Iye analalikira uthenga wodabwitsa wa chipulumtso, wa Mzimu Woyera komanso Ufumu wa Mulungu. Uthenga wabwino unafalikira kwa anthu onse, Ayuda ndi Agriki omwe ku madera onse a Asia Minor (kumene masiku ano kumadziwika kuti dziko la Turkey). Uthengawu unatsimikizidwa ndi machiritso komanso mamasulidwe, ndipo mphamvu ya Mulungu inali pa Paulo modabwitsa mwakuti iye amapempherera ndi kud zodza mipango imene kenaka imatengedwa kwa odwala ndiponso ogwidwa ndi mizimu yoipa. Odwalawo amachiritsidwa ku matenda ao ndipo iwo amene anali ndi mizimu yoipa amamasulidwa.

Panali Ayuda ena amene amatulutsa ziwanda ndipo amayendayenda kulikonse kufuna kutulutsa mizimu yoipa ndi kuchiritsa matenda pogwiritsa ntchito zithumwa ndiponso pobwebweta. Pamene iwo anamva za mmene Paulo anatulutsira ziwanda m'dzina la Yesu, iwo anaonjezapo dzina limenelo ku mndandanda wa zimene amanena ndiponso kuchita. Kwa anthu amene anali ogwidwa ndi ziwanda, iwo aja amati: "Ndikulumbirirani pa Yesu amene amlalika Paulo, tulukani!" Skeva, anali wansembe wotchuka pakati Ayuda, ndipo anali ndi ana asanu ndi awiri amene amasirira mphamvu imeneyo. Iwo atomva za Paulo komanso mphamvu imene inali mwa iye m'dzina la Yesu, ana aamuna asanu ndi awiri aja anamuzungulira munthu amene anagwidwa ndi mzimu woipa. Modzionetsera ndi kugwiritsa ntchito ulamuliro wobwerekera,

iwo anaika manja pa munthuyo nalamulira kuti, "M'dzina la Yesu, tuluka!"

Mzimu woipa mkati mwa munthuyo unalankhula kuti: "Yesu ndimzindikira, ndi Paulo ndimdziwa, koma inu ndinu ayani?" Mwanjira ina tikhoza kunena kuti, "Ndikudziwa za ulamuliro wakumwamba wa Yesu komanso mphamvu zimene zili mwa mtumiki wake Paulo, koma inuyo mulibe kulumikizana kulikonse ndi Mulungu ndiponso mulibe ulamuliro pa ine. Mukuganiza kuti ndinu ayani?" atatero, mzimu woipa unachoka mwa munthuyo ndi kuwadumphira anyamata asanu ndi awiri aja amene amafuna kuwutulutsa. Mphamvu ya Satana inawaposa ndi kuwagonjetsa. Akulira ndi kudzimenya, akamunawo anakwinya nkhope ndipo amatuluka thovu kukamwa. Iwo anang'amba zovala zao kenaka nkutuluka chothawa m'nyumbamo ali amaliseche ndi ovulazidwa.

Pamene Ayuda ndi Agriki onse okhala ku Efeso anamva za nkhanayi, panagwa mantha aakulu pakati pao ndipo dzina la Yesu linachitidwa ulemu koposa. Anthu ambiri anavomereza zoipa zao m'miyoyo yao ndipo anapulumsidwa ku mphamvu ya uchimo. Iwo anabweretsa mabuku ao a zamatsenga, zobwebweta ndi zithumwa, ndipo anawaotcha onse m'chimoto chachikulu, pozindikira kuti sizinali za kwa Mulungu. Mau a Mulungu anakula chikulire pomwe ntchito za mdierkezi zinachititsidwa manyazi.

Kuwerenga Malemba a zinthu izi zodabwitsa ndi kolimbikitsa ndiponso kosilirika, koma zikuyenera kubweretsa mantha ndi kuopa Mulungu kwa munthu amene akuwerengayo.

(Yapitirira pa tsamba 2)



"Ndipo unayankha mzimu woipa, nuti kwa iwo, 'Yesu ndimzindikira, ndi Paulo ndimdziwa, koma inu ndinu ayani?' "

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Muli mphamvu m'dzina la Yesu, koma mphamvu imeneyo imapezeka kwa iwo amene adziwana ndi Mulungu kwathunthu ndipo ndi oonadi mu mtima wao. Satana mwiniwake amawadziwanso Yesu ndipo amawadziwanso atumiki enieni a Ambuye. Satanayo amawadziwanso iwo amene sali opulumutsidwa. Iye amadziwa tchimo lobisika ndiponso choipa chilichonse chimene chili mumtima

mwa munthu. Iye amadziwa amene ali achiphamaso ndipo alaliki amene ali ngati ana a Skeva. Mzimu woipa unafunsa funso limene liyenera kufufuzidwa mwatsanetsatane ndi munthu wina aliyense. Kodi ndinu ndani? Kodi mumadziwika motani? Kodi ndi zoona zotani zimene zimafotokoza zenizeni za chikhalidwe chanu.

Anthu ambiri amadziwika ndi dzina lao, mtundu wao, mtundu wa khungu lao, chipembedzo chao, mpingo wao kapena udindo wao. Zinthu izi ndi zosafunikira pamene muzifananiza ndi kudziwika kwa kuuzimu. Kudziwika kwa kuuzimu sikudalira udindo wa kuuzimu kapenanso udindo wa utsogoleri mu mpingo.

Kodi ndinudi mwana wa Mulungu, amene mukukhala m'moyo wa chiyero tsiku ndi tsiku mosadukiza ndi cholinga chofuna kukondweretsa Ambuye? Kodi mumadzitchula nokha kuti ndinu Mkhristu ndipo mwina mumasonkhana ndi anthu a Mulungu, komabe muli ndi uchimo m'moyo mwanu? Kodi mumaoneka achiyero pa tsiku lamulungu koma mumachita ndi kuvala ngati munthu wachikunja mkati mwa sabata? Kodi muli ndi chimwemwe cha kwa Ambuye? Kodi mumanena zoona zokhazokha kapena ilipo nthawi imene mumanena bodza?

Kodi mumaoneka ngati mwamuna kapena mkazi okonda, koma mumazunza mnzanu wa banja pamene muli awiri mnyumba? Kodi mumathawa zoipa pamene kuli masana koma panthawi ya usiku mumatsatira zoipa zathupi zomwezo? Chimene timadziwika nacho kwenikweni sichifotokozedwa ndi zimene ife tinali kale kapena zimene tikufuna tidzakhale. Kodi ndinu ndani tsopano?

Tsiku lina, munthu aliyense adzaima pamaso pa Mulungu ndipo adzaweruzidwa molingana ndi kudziwika kwenikweni kwa uzimu wake. Tiyeni tsopano tidzisanthule mitima yathu ndiponso kufunsa funso lakuti: "Kodi ndine ndani kwenikweni kuuzimu?" ■


Koma iye wakuponyerera m'lamulo langwiro, ndilo lafulu, natero chiponyerere, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakuchita ntchito, adzakhala wodala m'kuchita kwake.

—Yakobo 1:25

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muyankhe email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya Gospel Truth imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org



Mau a Mkonzi



Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu. —Aefeso 4:13

Pamene munthu wapulumutsidwa ndi mwazi nayeretsedwa ndi Mzimu Woyera, iyeyo amayenerezedwa kuti akhoza kutumikira Ambuye mu chiyeero. Nthawi zonse padzakhala zinthu zakuti Ambuye

akuzikonza komanso madera amene mwana wa Mulungu akuyenera kuti akulemo. Cholinga chathu ndicho kukhala ngati Yesu pamene tsiku ndi tsiku tikudzikhuthula ndi kudzipereka tokha ku chifuniro cha Mulungu. Amene ali woyera mtima wa Mulungu sakuyenera kuopa kuvomereza kuti walakwa kapena kuti ali ndi chofooka. Pamenepo ndi pomwe tikhoza kupeza chipambano ndi mphamvu zochuluka. Musakhumudwe pamene Ambuye akuwululirani chosowa cha uzimu. Chimenecho chimakhala chili chifundo ndi chikondi cha Mulungu chikutithandiza kuti tikonzekere kuweruzidwa.

Ulendo uno, mutu umene tikulingalira si wokhudza zina za umulungu popeza kwakukulu ndi wongofuna kulimbikitsana. Mtolo umene ndili nawo ndi wofuna kugawana nanu ena mwa Malemba amene akukhudzana ndi kudzisanthula. Ndi kovuta kuti tikhoza kudzioneka tokha, popeza anthu ambiri amafuna kudzioneka okha ngati abwino. Sitingathe kukula mwa Khristu ngati sitili okonzeka kusanthula miyoyo yathu ndi kukhala oona pa zofuna zimene zilipo. Mulungu sadzatifunsa kuti tisinthe chinthu chinachake popanda kutipatsa chisomo ndi kuthekera kwakuti tikhoza kusintha.

Dziko lathu ladzaza ndi anthu amene amatchula dzina la Khristu koma ndi kumakhalabe mu uchimo. Kodi chingachitike ndi chiyani aliyense atati adziyese miyoyo yao ndi Mau a Mulungu posanyengezera kapena kunamizira anthu ena? Anthu ochimwa akuyenera kuzindikira uchimo wao, koma ulendo uno nkhwawa yanga kwambiri ili pa anthu amene amadzinena kuti iwo ndi oyera mtima koma nkumakhala moyo umene sukufanana ndi Mau a Mulungu. Palibe aliyense wa ife amene sayenera kulangizidwa ndi Mau a Mulungu. Anthu ambiri amachita ngati kuti iwo akhoza kukhazikitsa malamulo ndi miyezo yaoyao ndipo iwo amatenga Mau a Mulungu ndi kungowalowetsa mkati mwa zimene iwo amakhulupirira. Mulungu sasintha, koma ifeyo ndi amene tikuyenera kuti tisinthe molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Apa ndipo pamene timapeza mtendere ndiponso kukhutitsidwa kwenikweni pa kutumikira Ambuye. Ndi chinthu chomvetsa chisoni kunena kuti ndiwe mwana wa Mulungu koma ndi kumabisa choipa, numaganiza kuti palibe amene achidziwe. Ndi zomvetsa chisoni kuti anthu sakumachita manyazi ndi chikhaliidwe chakudziko ngakhale pakati pa anthu a Mulungu.

Ngakhale kuli kofunikira kuwunikira ziphunzitso ndi zikhulupiro zathu, nkofunika kwambiri kuwunikira zikhaliidwe zathu komanso zimene timakonda. Anthu akhoza kukhala ndi ziphunzitso zabwino pamene Mulungu sakondwera ndi kakhalidwe kao ndiponso zinthu zimene zili m'moyo wao. Tiyeni titsekule mitima yathu kwa Mzimu wa Mulungu. Tiyeni timvere pamene tiwerenga Baibulo ndiponso kumva mauthenga ochokera kwa atumiki odzozedwa a Mulungu. Pamene tikusanthula moyo wathu ndi kutsatira Khristu, tidzamudziwa Iye kwambiri komanso chidzalo chake.

Michael W. Smith

January 2018

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Kalozera posanthula Mau a Mulungu

Mutu: Kudzisanthula wekha

Kuwerenga Malemba: Dziyeseni nokha, ngati muli m'chikhulupiro, dzitsimikizeni nokha. —2 Akorinto 13:5a

Tanthauzo: Kudzisanthula wekha ndiko kuphunzira ndi kudziunika khalidwe, zokonda, machitidwe, zokhumba ndi zolingalira za mumtima.

Mwachidule: Nkofunika kusanthula moyo wathu wauzimu kupanda apo tikhoza kudziyesera abwino ndipo tikhala a chiphamaso, tidzinyenga ndipo pameto ake sitikalowa kumwamba.



I. Dzisanthule wekha

- A. 2 Akorinto 13:5 Akutilangiza kuti tidzisanthule.
- B. 1 Akorinto 11:27-31 Dziweruzeni nokha.
- C. Masalmo 77:6 Santhulani mwakhama.

II. Kufunikira kwa Kudzisanthula wekha

- A. 1 Akorinto 10:12 Kuopa kuti mungagwe.
- B. Aroma 14:12-13 Kuti mudzipereke kwa Mulungu.
- C. Miyambo 21:2 Olondola m'maso anu.
- D. Agalatiya 6:7-8 Zotsatira mpaka muyaya.
- E. 1 Akorinto 6:9-11 Chisalungamo chikudzudzulidwa.

III. Kudzinamiza wekha

- A. Miyambo 30:12 Oyera m'maso a inu eni.
- B. Yakobo 1:22-25 Wokumva koma nkuiwala.
- C. Agalatiya 6:3-4 Kudzikuza kumanyenga.
- D. Mateyu 7:1-5 Chotsani mtandawo.

IV. Kudziyenereza wekha

- A. Miyambo 20:6-7 Kulengeza za ubwino wa iwe mwini.
- B. Luka 16:15 Mudzilungamitsa nokha.
- C. 2 Akorinto 10:17-18 Kudziyenereza.
- D. Mateyu 3:7-9 Musakhulupirire zimene mwakhazikikamo.

V. Odzilungamitsa okha

- A. Mateyu 5:20 Sadzalowa Kumwamba.
- B. Mateyu 23:2-8 Iwo amanena koma sachita.
- C. Mateyu 23:23-29 Achiphamaso. Achiyero choonekera kunja.

VI. Zinthu zobisika

- A. Yohane 3:19-21 Kuwala kumavumbulutsa.
- B. Mlaliki 12:13-14 Mulungu adzalanga.
- C. Miyambo 28:13 Kubisa machimo.

VII. Mudziweruze nokha ndi chipatso chanu

- A. Miyambo 20:11 Mwana amadziwika chifukwa cha zimene amachita.
- B. Mateyu 7:13-23 Mtengo wabwino umabereka chipatso chabwino.
- C. Yohane 10:27 Nkhosa zimatsatira Mbusa.
- D. Tito 2:7-8 Onetsani ntchito zabwino.
- E. Mateyu 25:33-46 Ntchito zabwino.

VIII. Santhulani munthu yense

- A. Yohane 21:15 Kodi ndi chiyani chimene mumachikonda koposa?
- B. 1 Akorinto 6:20 Lemekezani Mulungu mu thupi ndi mzimu.
- C. 2 Mbiri 25:1-2 Chotifulumiza kuchita zinthu komanso mtima.

IX. Funafunani kuti Mulungu akuweruzeni

- A. Masalmo 26:2 Ndisanthuleni, O Ambuye.
- B. Masalmo 139:23-24 Ndiwuniken, O Mulungu.

X. Vomerezani zosowa

- A. 2 Samuele 12:7 Inu ndinu munthuyo.
- B. 2 Samuele 12:13 Ndachimwa.

XI. Khalani opanda chokaikitsa pamaso pa Mulungu


- A. 2 Akorinto 7:10-11 Khalani opanda chokaikitsa.
- B. Machitidwe 24:16 Chikumbumtima changwirowo.
- C. 2 Akorinto 7:1 Chiyero chikhale changwirowo.
- D. 2 Petro 3:18 Kulani m'chisomo.

Kumaliza

Popeza izi zonse zidzakanganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'chipembedzo. —2 Petro 3:11

Ubwino wa KUDZISANTHULA WEKHA

Pozindikira kuti tsiku la chiweruzo likubwera, Malemba amaikapo mtima kwambiri pa kudzisanthula kwa makhalidwe, machitidwe ndi zimene zimamufulumiza munthu kuchita zinthu. Nkwabwino kuti tidziyzedwa ndi Mau a Mulungu m'moyo uno pamene tili ndi mwai wakuti tikhoza kusintha, kusiya ndi kudikira mpaka pa tsiku la chiweruzo pamene mudzakhale kuti mwachedwa.



“Popanda
kudzisanthula
wekha mu kuopa
Mulungu, munthu
akhoza kudzinamiza.
Sikokwanira
kungomva
Mau kokha,
tiyenerakukhala
anthu ochita
Mau apo ayi
tinyengedwa.”

“Chotero munthu aliyense wa ife adzadziwerengera mlandu wake kwa Mulungu.” (Aroma 14:12). Tsiku lina, tonse tidzayenera kuimirira pamaso pa Mulungu pa tsiku la chiweruzo ndiponso ndi kupereka mndandanda wa zimene tachita ndi moyo wathu panthawi imene tinali padziko pano. Sitidzaweruzidwa potsatira mmene aliyense anachitira kapenanso zinthu zimene tinakumana nazo. Tidzaweruzidwa potsatira mmene mtima wathu uliri komanso zisankho ndi makhalidwe amene tinachita pa moyo wathu tsiku ndi tsiku.

Dzisanthuleni nokha

Ngakhale kuti kosavuta kuona zochimwa ndi zofooka za anthu ena, Paulo analimbikitsa mpingo wa ku Korinto kuti “Dziyeseni nokha, ngati muli m’chikhulupiriro, dzitsimikizeni nokha.” (2 Akorinto 13:5). Musangoona miyoyo ya anthu ena koma

mudzisanthule moyo wanu ndi chikhulupiriro chanu. Santhulani mtima wanu ndi mzimu wanu (Masalmo 77:6) ndipo tsimikizani kukhulupirika kwanu kwa Mulungu. Tonsefe ndife anthu ndipo timalakwitsa ndi kusiya njira yoyenera ngati sitikhala ndi nthawi yapadera ya kudzisanthula. Chifukwa chakuti munthu wina wake wakhala akutumikira Ambuye kwa zaka zochulukana, izi sizitanthauza kuti munthuyo lero akuyenda m’moyo wokondweretsa Mulungu. “Chifukwa chake iye wakuyesa kuti ali chilili, ayang’anire kuti angagwe” (1 Akorinto 10:12).

“Njira zonse za munthu zilungama pamaso pake; koma Yehova ayesa mitima.” (Miyambo 21:2). Nkosavuta kwa munthu kuganiza kuti iye ndiye akukhoza ndipo ena onse akulakwa kusiya ndi kuti adzisanthule moyo wake. Mulungu akugwira ntchito yowunika osati ntchito zathu zokha, koma ngakhale mitima yathu imene. Chifukwa chake nchanzeru kuti tisanthule miyoyo yathu moona mtima kuti potero tikhale chimene Mulungu

akufuna osati chimene thupi lathu lavomereza kuti ndicho cholondola. Chilichonse chimene tibzala m’moyo uno tidzakolola m’moyo wosatha. Tisanyengeke, sitingathe kumupusitsa Mulungu, popeza Iye amadziwa zinthu zonse. (Agalatiya 6:7-8). Malemba amatiphunzitsa momveka bwino pa 1 Akorinto 6:9-11 kuti osalungama sakalowa Kumwamba. Onse adama, opembedza mafano, achigololo, olobodoka ndi zoipa, akudziipsa ndi amuna, osirira, oledzera, olanda ndi ena otere adzavutika kwamuyaya pokhapokha atembenukire kwa Mulungu nayende m’moyo wangwiro. Dziko ladzaza ndi anthu onena kuti iwo ndi Akhristu koma akuchita machimo awa. Pokhapokha atalapa, mapeto ake ndi odziwika kale. Pali mbadwo umene ndi woyera m’maso mwawo, koma sunatsukidwe ku chidetso chake. (Miyambo 30:12).

Kuopsa kwa Kudzinamiza

Popanda kudzisanthula wekha mu kuopa Mulungu, munthu akhoza kudzinamiza. Sikokwanira kungomva Mau kokha, tiyenerakukhala anthu ochita Mau apo ayi tinyengedwa. (Yakobo 1:22-25). Kungodziwa chabe za choonadi komanso kuyanana ndi anthu a Mulungu pazokha sizitikonzeke kutsutsa kukhala oweruza. Ena mwa anthu amene amakonda kutsutsa zinthu ndiwo omwe amene ali ndi chintanda m’maso mwao. “Tayamba kuchotsa m’diso lako mtandawo, ndipo pomwepo udzapenyetsa kuchotsa kachitsotso m’diso la mbale wako” (Mateyu 7:1-5).

Kanani kudziyenereza

Kuyenda m’moyo wangwiro ndi wokhulupirika ndi mdalitso waukulu. Kumeneko kuposa onse amene amanena za ubwino wao (Miyambo 20:6-7). Ntchito kapena ukatswiri pa chinthu sizipulumutsa komanso kudzikuzira muuzimu sikubweretsa mphamvu kuchokera kwa Mulungu. Yesu anatani: “Inu ndinu odziyesera nokha olungama pamaso pa anthu; koma Mulungu azindikira mitima yanu.” (Luka 16:15). Kudzisanthula sikutanthauza kudzilungamitsa, “pakuti si iye amene adzitama yekha, koma iye amene Ambuye amtama ali wovomerezeka” (2 Akorinto 10:18). Anthu ambiri anamizira kuchita zinthu m’moyo wao zimene Mulungu samavomereza. Ena amadalira dzina la banja lao, mtundu wao, mbiri kapena kudziwika kwa mpingo wao, kapenanso udindo umene ali nao mu utsogoleri. Yohane Mbatizi anawauza Afarisi kuti: “ndipo musamayesa kunena mwa inu nokha, Atate wathu tili naye Abrahamu” (Mateyu 3:9). Iwo amadzitenga kuti anali olungama chifukwa anali zidzukululu za anthu a Mulungu akale amene anali oyera. Tikhoza kukhala ndi makolo kapena

(Yapitirira pa tsamba 6)



**“Pamene anthu
akhala oona ndi
omasuka pamaso
pa Mulungu,
padzakhala ndithu
kukula mu uzimu
kopitirira.”**

(Kuchokera pa tsamba 5)

anganga amene anali kutumikira Mulungu. Tikhoza kumapembedza nao ndi mpingo wa “Church of God,” komabe izi sizitipulumutsa kapena kuyeretsa choipa chimene tingamachite m’moyo wathu.

Yang’anani mkatimo

Maonekedwe akunja a chipembedzo satipulumutsa. “Ngati chilungamo chanu sichichuluka choposa cha alembi ndi afarisi simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba” (Mateyu 5:20). Pa Mateyu 23:23-29 Yesu analankhula kwambiri za kudzilungamitsa kwa atsogoleri a chipembedzo a nthawi imeneyo. Iwo amalankhula mau oona koma samatsata malamulo a Mulungu. Iwo amavala monga anthu achiyero pamene mkati mwao amachita zathupi ndiponso anali odzaza ndi chinyengo. Yesu anati iwo anali achiphamaso. Kuvala kodzipatsa ulemu ndi kofunikira ndipo kumafunika kuwunikiridwa,

koma kopoa zonse munthu wamkati asanthulidwe. Pali anthu amene amaoneka opembedza m’maonekedwe akunja koma pamene mkati mwao ndiwo aliuma, odzikuza, odana ndi anza. Dzisanthuleni nokha.

Palibe chobisika

Tiyenera kudziyeza molingana ndi kuwala kwa choonadi ndipo tisakhale pansi pa mdima, tisadzilungamitse kapena kudziyenereza. Mulungu adzaweruza chinthu china chilichonse chobisika (Mlaliki 12:13-14). Dzisanthuleni nokha moyo wanu ndipo musanamizire chilichonse chimene sichili cha umulungu. Pamene anthu abisa machimo ao, sadzapambana. Koma pamene awavomereza ndi kuwasiya, Mulungu adzawachitira chifundo. (Miyambo 28:13).

Amadziwika ndi chipatso chake

Pa Miyambo 20:11 timawerenga kuti: “Ngakhale mwana adziwika ndi ntchito zake; ngati ntchito yake ili yoyera ngakhale yolungama.” Monga mwana amadziwika, ifenso tidziwike ndi choonadi m’zochita zathu. Kodi inu mukubereka chipatso chanji? Yesu ananena kuti mtengo wabwino umabereka chipatso chabwinonso (Mateyu 7:16-23) ndipo monga anthu ena tidzawadziwa chifukwa cha chipatso chao—nafenso tikuyenera kuzidziwa. Ndi mdalitso waukulu kudzisanthula tokha ndi kuonamo mwa ife chipatso chabwino. Komabe, Yesu anachenjeza za nkhandwe mkati mwa nkhoa. Pali atumiki ambiri pakati pathu amene akulalikira komanso kuchita zamphamvu m’dzina la Mulungu, koma kunena zoona, iwo ndi nkhandwe zamuuzimu. Nkhosa zenizeni zimakhala ndi kulimba mtima komanso

chitetezo pamene zisanthula moyo wao, popeza nkhosazo zimadziwa ndi kutsatira liwu la mbusa (Yohane 10:27).

Santhulani thupi ndi mzimu

Munthu yense, wamkati ndi wakunja yemwe, akuyenera kusanthulidwa. Yesu anafunsa Petro kuti: “kodi undikonda Ine koposa awa?” (Yohane 21:15). Kodi inuyo mumakondadi Mulungu koposa kalikonse ka m’dziko lapansili? Kodi mukungofuna zinthu zadziko lino kapena Khristu ndiye oyamba m’moyo wanu? Pa 1 Akorinto 6:20 tikulangizidwa kuti tidzilemekeza Mulungu mu m’thupi lathu ndi mzimu wathu. Pamene anthu ayang’ana mu galasi, amadziona mmene akuonekera. Anthu akuyenera kuyang’ana mu galasi la uzimu komanso kusanthula zenizeni zokhudza uzimu wao, asanthule moyo wao molingana ndi muyeso wa Mau a Mulungu.

Funani chiweruzo cha Mulungu

Mfumu Davide anatipatsa ife chitsanzo mu pemphero lake kangapo konse. “Mundisanthule, Mulungu, nimudziwe mtima wanga; muniyese nimudziwe zolingalira zanga” (Masalmo 139:23-24). Pamene Davide anadzudzulidwa ndi mneneri Natani chifukwa cha tchimo lomwe anachita, iye anavomereza tchimo lakelo ndipo anapempha chikhululuki. Tiyeni titsekule mitima yathu kuti Mulungu atisanthule ndi kutionetsa ife chilichonse chimene chili chotsutsana ndi Khristu. Likhoza kukhala kuti sitchimo koma choofoka chinachake chimene chikutchinga moyo wathu wauzimu kuti usapite patsogolo. Dzisanthuleni nokha ndipo pezani chigonjetso povomereza choipacho kenaka ndi kusingha.

Mtima wofunitsitsa

“Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okondedwa, tidzikonzere tokha kuleka chodetsa chonse cha thupi ndi cha mzimu, ndi kutsiriza chiyeero m’kuopa Mulungu.” (2 Akorinto 7:1). Dziyeretseni pamaso pa Mulungu ndipo tsiku ndi tsiku mudzipime nokha monga Paulo kuti “ndikhale nacho nthawi zonse chikumbu mtima chosanditsutsa cha kwa Mulungu ndi kwa anthu” (Machitidwe 24:16). Pokhala anthu amene tili oona mtima ndi osabisa kanthu kwa Mulungu, tidzakhaleba tikukula m’moyo wathu wauzimu.

Chimwemwe pamene tigonjera kwathunthu

Pali mtendere wodabwitsa umene umakufikirani pamene mwadziwa kuti machimo anu akhululukidwa, mtima wanu ndi woyera ndipo chokhumba chanu ndicho kukondweretsa Mulungu. Ndi umboni wodabwitsa pamene tidzatha kunena monga Yesu ananena zokhudza Satana kuti: “ndipo alibe kanthu mwa Ine” (Yohane 14:30).

Pamene tadziwa kuti nthawi yayandikira, tikhale anthu otani kodi? Tisaope kudzisanthula tokha, popeza pali Mulungu amene ali wokonzeka komanso akuyembekezera kuti atumikire ku zofuna za moyo wathu. ■

Funso

?

Yankho

Kodi mungathe kupereka tanthauzo la “nyanja yagalasi” monga akunenera pa Chivumbulutso 4:6?



Malemba amanena kuti: “ndipo kumpandowo, ngati nyanja yagalasi yonga krustalo; ndipo pakati pa mpandowo, ndi pozinga mpandowo, zamoyo zinai zodzala ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo.”

Chivumbulutso 15:2 amakambanso za nyanja yagalasi ndipo nkhanu yake ndi yofanana ndi yomweyi. Tikayiunika bwino nkhanu, mu mavesi owonjezerawo, akukamba za kukongola ndi ulemmero wosaneneka wa Mulungu ali pa mpando wake wachifumu. Anthu oyera mtima onse a Mulungu anazungulira pampano wachifumu, namalambira ndi kutamanda Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse. Ndime zimenezi nzofunika kuziphunzira bwino ndiponso kuzimvetsetsa, koma pano tingonenapo za funso limene tafunsali.

Nyanja yagalasi inali ngati mwala wonyezimira wa krustalo ndipo inayala ponse pozungulira mpando wachifumuwo. Imaoneka yowala, yosalala ndiponso yoonekera mkati mwake. Anthu a Mulungu oombedwa anaimirira pa nyanjayi ndi kumalambira Mulungu. Izi tisazitenge kuti zimachitikadi choncho koma akungotipatsa

chithunzithunzi. Nkofunikira kudziwa kuti pozungulira mpandowo pali nyanja yagalasi—imene ili yosadetsedwa, yoyera mbee! yopanda banga ndi yoyeretsetsa. Zimenezi zikuimira choonadi, chiyero ndi kusabisa kanthu. Mpingo weniweni wa Mulungu umaimira kupanda banga kapena chodetsa, ndipo umakhala mu choonadi ndi chikondi.

Oyera mtima a lero, ngakhale ali pansi pano, akuyenera kuimira pa nyanja yagalasi pamene palibe chodetsa kapena chobisika. Ife ndife amene timanena chimene tili ndipo sitifunikanso kuti tidzilungamitse, tidzibise kapena tinamizire kusalungama. Ngati Akhristu, mipingo kapena atumiki a Mulungu sakufuna kuti zimene akuchita zisamaonekere, ndiye kuti pali vuto lalikulu ndicho chinachake chalakwika. Tiyezi tikweze mau athu ndi mayamiko komanso chiyero ndipo tiimirire mu chilungamo cha Mulungu ndi choonadi komanso popanda china chotitsutsa. ■

Kalozera podzisanthula

Kodi ine...



Ndikukonda Mulungu ndi mtima wanga wonse?

NTHAWI
ZONSE

☐

NTHAWI
ZINA

☐

AYI
M'PAN'GONO
POMWE

☐

Ndikumvera Ambuye m'magawo onse a moyo wanga?

☐
☐
☐

Ndikulankhula ndi mau a chisomo komanso achikondi?

☐
☐
☐

Ndikuvala modzilemekeza komanso mosadzikometsera kwambiri?

☐
☐
☐

Ndine wodzichepetsa pa mmene ndimadzionera?

☐
☐
☐

Ndine wokhulupirika pakupita ku tchalichi kukapembedza?

☐
☐
☐

Chilipo chimene ndikuyesetsa kuchibisa m'moyo wanga?

☐
☐
☐

Ndikuonera kapena kumvera zinthu zimene ndikhoza kuchita nazo manyazi atakhala kuti Khristu ali pompo?

☐
☐
☐

Ndine wokangalira pa kupemphera ndi kuwerenga Baibulo?

☐
☐
☐

Ndimadzionetsa woyera kunyumba monganso mmene ndimachitira ku tchalichi?

☐
☐
☐

Ndikuonetsera mzimu komanso chiyero cha Khristu?

☐
☐
☐




KODI MUKUDZIWA?

Mu Baibulo, pamene Yesu amagwiritsa ntchito mau akuti “wachiphamaso” mauwa amanena zambiri zimene timadziwa masiku ano—munthu amene amanena zina koma nachita zinthu zina, wa makhalidwe awiri. Tsinde la mauwa mu Chigriki

limatanthauza “wochita zisudzo.” Wazisudzoyo, pamene watenga khalidwe lina

mu sewero, amachita izi pofuna kuti asangalatse owonerera komanso kuti amuchemerere. Komatu pamene palibe amene akuona, ndipo aliyense wapita, wochita zisudzo uja amabwerera ku moyo wake weniweni umene nthawi zambiri umakhala wosiyana ndi womwe anali nawo pa nthawi yachisudzo ija.



**Mau a
Nyengo
Yake**

MULANDIRANE WINA NDI MNZAKE

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Chifukwa chake mulandirane wina ndi mnzake, monganso Khristu anakulandirani inu, kukachitira Mulungu ulemmerero. —Aroma 15:7

Khristu akukulitsa ubale ndi ubwino wake kwa anthu a maiko onse, zilankhulo zonse ndi mitundu yonse. Iye walandira anthu ochokera kosiyanasiyana komanso ochita zosiyanasiyana. Khristu anatilandira ife tikadali osweka ndi aumphawi choncho. Mwachikondi chake, Iye anatsika ndi kutipeza ife tikadali otayika natidzutsa ndi chisomo chake. Ngakhale kuti chipulumutso chimabweretsa kusintha kwakukulu pa moyo wathu, anthufe ndife osiyana kachitidwe ka zinthu komanso zimene timakonda. Ngakhale izo zili choncho, Khristu amatilandirabe nativomera kuti ndife ake chifukwa cha chikondi chake chachikulu. Sitilinsu anthu otayidwa kunja kapena achilendo koma ndife mbadwa za mu Ufumu wa Mulungu.

Monga Khristu anatilandira, ifenso tikuyenera kulandirana wina ndi mnzake. Tiyenera kutsekula mitima yathu kwa akhristu anzathu ndi kuwaonetsera chikondi komanso kuwalemekeza monga abale ndi alongo mwa Ambuye.

Khristu sanatilandire tili angwiro koma tili amphulupulu chomwecho. Nanga tingachitenso chiyani chachikulu kuposa apa? Tiyenera kusamalirana wina ndi mnzake

komanso kuonetserana chikondi chakumwamba ndiponso kulandirana kusiyana ndi kuti tilemberane malire chifukwa cha kusagwirizana pa zinthu zazing’ono zokhudza zimene timaganiza ndi kukhulupirira. Ngati Khristu akadati adzitolandira monga mmene ife timachitira ndi ena pa zinthu zauzimu, kodi ife tikadakhale oyanjana ndi Mulungu?



Sitiyenera kunyozana kapena kuwanyogodola akhristu ena ngati tikuona kuti iwowo ndi ofooka mu uzimu kapena kumvetsetsa kwao ndi kocheperapo. Paulo anatilandira kuti, “Ndipo iye amene ali wofooka m’chikhulupiriro, mumlandire, koma si kuchita naye makani otsutsana ai” (Aroma 14:1). Paulo amatanthauza za Ayuda amene anatembenuka mtima komabe amakhazikikabe pa miyambo ina ya mu Lamulo lakale. Langizo lake linali lakuti iwo alandiridwe komanso awalole kuti akhale nawo pa chiyanjano popembedza. Iye anapitiriza kulangiza oyera mtima onse kuti awalandire Ayudawo popanda chikaiko chilichonse. Sakuyenera kuwasala kapena kungowavomera ndi cholinga chofuna kuwadzudzula kapena kuwanena mowanyoza. Awalandire mwachikondi ndi mokoma mtima.

Ndi zinthu zodabwitsa kuti pakati pa ena mwa ana a Mulungu, anthu awiri akhoza kumaonana ngati kuti wina aliyense wa iwo ndi ofooka mu chikhulupiriro. Pakati pa kagulu kena ka okhulupirira, pali kachizolowezi komayang’anirana pansi ndiponso kukaikirana. Malemba amatiphunzitsa kuti tikhale okonzeka kulandirana osati kutayana kunja. “Mulandirane wina ndi mnzake.” ■